Kunali azimayi ambiri amaganizo ngati anuwo...

Mphatso

Mphatso anali kukhala pa mudzi wina waung'ono. Iye sanathe kutsiriza sukulu yake chifukwa chosowa ndalama. Mwamwayi, mayi wina wake anamulemba ntchito mu hotela ku Lilongwe. Mphatso anakongola ndalama zoyendera ndipo anafikadi ku Lilongwe. Koma m'malo mwa ntchito yabwino ya ndalama zambiri, iye adapatsidwa ntchito yowawa ya malipiro ochepa kwambiri. Kuti abweze ngongole ija ndikuthandiza achibale ake ndi ndalama, Mphatso anayenera kusanduka hule.

Memory

Memory analowa nawo m'bungwe lolemberana makalata pofunafuna kupeza mwamuna wolemera wa dziko lakunja. Bwenzi lolemberana nalo makalatalo lidamuitanitsa kupita ku Germany, ndendende ndi m'mene iye ankafunira. Koma iye atangofika, anatayiratu mtima. Amene ankati adzakhala mwamuna wakeyo sanali chidakwa chabe komanso anali ogona m'bala ndipo ankangokhalira kumuzunza.

Thereza

Mlendo wa ku Belgium adaalonjeza Thereza ntchito ya ukalaliki mu hotela yake. Koma atakafika kumeneko, mwamunayo adamulanda chiphaso chake choyendera ndipo adamuumiriza kugwira ntchito yogonana ndi amuna osiyanasiyana.

NGATI MULI KALE M'MAVUTO, PALI MABUNGWE OMWE ATHA KUKUTHANDIZANI

KU MALAWI...

CENTRE FOR SOCIAL CONCERN (CFSC)
P.O. Box 40049
LILONGWE 4, MALAWI
TEL. 01 715 632 / 01 715 450

CATHOLIC WOMEN ORGANISATION (CWO)
KU PARISH ILIYONSE

CATHOLIC COMMISSION FOR JUSTICE & PEACE (CCJP)
KU PARISH ILIYONSE

ASSOCIATION OF RELIGIOUS WOMEN OF MALAWI (ARIMA)
KU DAYOSIZI ILIYONSE

MAIKO AKUNJA...
KU POLISI YAPAFUPI NANU

Funsani zambiri ndi chithandizo kwa munthu amene wakupatsani chikalata chino

Design & Print @ Montfort Media, Balaka - 01 545 267

CHENJEZO KWA INU AMAYI

MOYO WABWINO POPITA KU MABOMA ENA KAPENA KU MAIKO AKUNJA?